ife ku mitima yathu yoyipa.



PHUNZIRO LA 62

1. Kodi chifukwa chiyani Yesu sanapite nthaŵi yomweyo kwa Lazaro atamva kuti iye akudwala?
-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuti awonetse mphamvu zache zopambana ngati Mulungu Mpulumutsi.

2. Malita ankaganiza kuti Yesu adzamudzutsanso mulongo wache, Lazaro, pa tsiku lomaliza.
-Kodi Yesu ankatanthawuza zimenezi?
-Ayi.

3. Kodi Malita ankatanthawuza chiyani ponena kuti Tsiku lomaliza?
-Pa tsiku lomaliza lidzakhala tsiku limene anthu onse akufa adzawukenso kumanda kuti adzaweruzidwe ndi Mulungu pa machimo awo amene akhala akupanga.

4. Kodi chifukwa chiyani Lazaro sayenera kuyembekezera pa tsiku lomaliza kuti awukitsidwe ku imfa?
-Chifukwa chakuti Yesu anali pomwepo, ndipo Iye ndi Kuwuka ndi Moyo.

5. Kodi ndi ndani yekha amene angapereke moyo kwa anthu akufa?
-Yesu amene ali Mulungu.

6. Yesu analankhula kuti aliyense okhulupilira mwa Iye adzakhalabe ndi moyo ngakhale amwalira.
-Kodi munthu angakhale bwanji ndi moyo atamwalira?
-Yesu ankatanthawuza kuti aliyense okhulupilira mwa Iye sadzafa pamaso pa Mulungu ngakhale kuti thupi lache lidzafe.

7. Kodi chifukwa chiyani Yesu analira atafika kumanda a Lazaro?
-Chifukwa chakuti Iye anadandawula kwambiri powona anthu ena akulira.

8. Kodi Yesu anatha bwanji kuperekanso moyo kwa Lazaro amene anamwalira?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi amene analenga moyo onse.

9. Kodi chifukwa chiyani Yesu anaganiza zopereka moyo kwa Lazaro amene anamwalira?
-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuti aŵawonetse anthu onse kuti Mulungu ali ndi mphamvu ngakhale pa imfa.

10. Kodi amene ankafuna kumupha Yesu anali ndani?
-Akulu akulu amsembe ndi Afarisi.

11. Kodi ankaŵatsogolera akulu akulu amsembe ndi Afarisi kuti amuphe Yesu anali ndani?
-Satana.

-Anthu ankakonda kupititsa ana awo kwa Yesu

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:13

13-Anthu ankapita nawo ana kwa Yesu kuti akaŵakhudze, koma ophunzira a Yesu anaŵadzudzula.

-Kodi chifukwa chiyani ophunzira a Yesu anaŵadzudzula anthu chifukwa chopita ndi ana awo kwa Yesu kuti akaŵakhudze?
-Ophunzira a Yesu ankaganiza kuti Yesu sankafuna kuti adzivutitsidwa ndi ana.



22-Koma nkhope yache inagwa chifukwa cha mawu aŵa. Ndipo iye anachoka ali wachisoni chifukwa chakuti anali ndi chuma chambiri.
23-Ndipo Yesu anawunguzawunguza nati kwa ophunzira ache, “Ndi kovuta kwambiri kuti munthu wa chuma adzaloŵe ku Ufumu wa Mulungu!”
24-Ndipo ophunzira achewo anazizwa ndi mawu ache. Koma Yesu anatinso, “Ananu, nkovuta ndithu kwa iwo amene akuchitama chuma kuloŵa mu ufumu wa Mulungu!”

-Kodi chifukwa chiyani mnyamata wa chuma uja anapita kwawo ali asakondwa?
-Chifukwa chakuti anali ndi chuma chambiri.
-Chifukwa chakuti sankafuna kuti apereke chuma chake chonse kwa osawuka.
-Chifukwa chakuti sankafuna kuti Yesu awusinthe mtima wache woyipa uja.

-Kodi anthu atamufunsa Yesu poyamba paja kuti kodi ayenera kuchita chiyani kuti akakhale ndi moyo osatha, Yesu anaŵayankha chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 6:28-29

28-Kenako iwo anamufunsa Iye kuti, “Kodi ife tiyenera kuchita chiyani kuti tidzigwira tchito zimene Mulungu akuzifuna?”
29-Yesu anayankha kuti, “Ntchito za Mulungu ndi izi: kukhulupilira mwa Iye amene anamutumizayo.”

-Ntchito yokhayo imene ife tiyenera kuyichita kuti tikhale ndi moyo osatha ndi yokhulupilira mwa Yesu Kilisitu.

-Yesu Kilisitu yekha ndi amene angathe kutipulumutsa

lumutse iwo ku mitima yawo yoyipa imene ili mkati mwawo.

-Kodi nanga Yesu analankhulanso chiyani kwa mnyamata wa chuma uja?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:21b

21b-[Yesu anati] “Pali chinthu chimodzi chimene ukuchisoŵa, “Pita ndipo ukagulitse china chilichonse chimene uli nacho ndipo uthandizire osawuka ndipo udzakhala ndi chuma kumwamba. Chomcho ukabwere kuno, udzanditsate Ine.”

-Kodi Yesu anamuwuza mnyumata wa chuma uja kuti akachite chiyani?
-Anamuwuza kuti akagulitse chuma chake chonse ndikukaŵapatsa osawuka ndipo adzamutsate Iye.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu analankhula zimenezo?
-Yesu ankadziŵa kuti munthu wa chumayo ankachikonda chuma chake kwambiri kuposa anthu osawuka.

-Yesu ankadziŵa kuti munthu wa chumayo ankachikonda kwambiri chuma chake kuposa Mulungu.

-Kodi ife ngati tikuchikonda chuma kwambiri kuposa Mulungu, Iye akatipulumutsa?
-Ayi.

-Kodi kenako mnyamata wa chuma uja anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:22-24



-Kodi Yesu anavutitsidwa ndi ana?
-Ayi.

-Kodi Yesu analankhula chiyani kwa ophunzira ache?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:14

14-Koma Yesu atawona izi, Iye anakwiya. Ndipo anati kwa iwo, “Lolani ana kuti adze kwa Ine, musaŵaletse, pakuti ufumu wa Mulungu uli wa otere.”

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anakwiya ndi ophunzira ache?
-Chifukwa chakuti ophunzira ache ankaŵaletsa anthu kuti asamapite ndi ana awo kwa Iye.

-Kodi Yesu amaŵakonda ana onse?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu amaŵakonda ana onse?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi amene anaŵalenga ana onse.

-Chifukwa chakuti Yesu ndi amene anaŵalenga ana onse, Iye amafuna kuti aŵapulumutse iwo.

-Ana nawonso amabadwa mu tchimo ngati akapolo a Satana.
-Ana nawonso akufunika kuti apulumutsidwe ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Ichi ndi chifukwa chake kuli kofunika kuti ana nawonso adzimvera Mawu a Mulungu.

-Kodi kenako Yesu analankhula chiyani za ana ndi Ufumu wa Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:15-16

15-[Yesu anati] “Ine ndikukuwuzani zowona, aliyense amene sawulandila Ufumu wa Mulungu ngati mwana, sadzaloŵa mu ufumuwo.”
16-Ndipo iye anaŵayangata ndi manja ache, naŵadalita, nayika manja ache pa iwowo.

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani pamene analankhula kuti aliyense amene sawulandila Ufumu wa Mulungu ngati mwana, sadzaloŵa mu ufumuwo?
-Yesu ankatanthawuza kuti ngati sitikukhulupilira mwa Mulungu ndi chikhulupiliro ngati cha mwana, sitidzapulumutsidwa.

-Kodi chikhulupiliro ngati cha mwana ndi chotani?
-Chikhulupiliro cha mwana chimakhala chenicheni.
-Chikhulupiliro cha mwana chimakhala cha mtima onse.

-Mwana akamayamwa bele la amache, amaŵakhulupilira amachewo ndi mtima wache onse.
-Mwana akabelekedwa pa msana wa amache, amaŵakhulupilira amachewo ndi mtima wache onse.

-Ngati m’mene mwana amaŵakhulupilililira amache ndi mtima wache onse, chomchonso Yesu anati kuti ife tiyenera kukhulupilira mwa Mulungu ndi mtima wanthu onse.

-Ngati sitikhulupilira mwa Mulungu ndi mtima wathu onse, sitidzapulumutsidwa.



amulo ache khumi kwa a Isilayeli?
-Kufuna kuŵatsimikizira kuti sanakaŵatha kuŵatsatira malamulo onse.
-Kufuna kuŵatsimikizira kuti mitima yawo inali yiodzadza ndi tchimo.
-Kufuna kuŵatsimikizira kuti mitima yawo inali yowola.
-Kufuna kuŵatsimikizira kuti iwo sanali anthu abwino.
-Kufuna kuŵatsimikizira kuti palibe munthu wabwino komo Mulungu yekha.

-Ngakhale titayesetsa kwambiri kuti tisunge malamulo onse a Mulungu panja, mitima yathu ndi yowolabe mkati mwathu.

-Ngakhale titayesetsa kwambiri kuti ntchito zathu zikhale zabwino, mitima yathu siyidzakhalabe yabwino pa maso pa Mulungu.

-Kodi kenako Yesu analankhula chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:21a

21a-Yesu anamuyang’ana iye, namukonda.

-Ngakhale kuti mnyamata wa chumayo sankamvetsetsa kuti mtima wache siwunali wabwino pa maso pa Mulungu, Iye anamukonda.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anamukonda mnyamata wa chumayu?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi amene anamulenga iye.
-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuti amupulumutse iye ku mtima wache oyipawo.

-Yesu anakonda anthu onse ndipo amafuna kuti aŵapu-

20-Ndipo iye anati kwa Iye, "Mphunzitsi, zonsezi ndakhala ndikuzisunga kuyambira ndili mwana.'

-Kodi mnyamata wa chuma uja anayankha chiyani?
-Anayankha kuti wakhala akuŵasunga malamulo a Mulungu kuyambira ali mwana.

-Kodi zimenezo zinali zowona?
-Ayi.

-Kodi pali munthu amene angathe kusunga malamulo onse a Mulungu?
-Palibe.

-Kodi chimene sankamvetsetsa mnyamata wa chuma uja ndi chiyani?
-Mnyamata wa chuma uja sankamvetsetsa zakuti, ngakhale kuti ankasunga malamulo a Mulungu onse panja, mtima wache umene unali mkati, unkaphwanyabe lamulo lililonse la Mulungu.

-Yesu anaphunzitsa kuti ngati munthu akumuda munthu nzache, wapalamula kale tchimo lakupha.

-Yesu anaphunzitsa kuti ngati mamuna akumuyang'na mkazi ndi kumukhumbira, wapalamula kale tchimo la chigololo mu mtima mwache.

-Kodi mukuchikumbukira chifukwa chimene Mulungu anaperekera malamulo khumi kwa a Isilayeli m'chipululu muja?
-Mulungu anadziŵa kale kuti a Isilayeli sanakatha kuŵasunga malamulo onse a Iye.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anapereka mal-



-Yesu atawuyamba ulendo wache, mnyamata wa chuma anafika kwa Iye ndikumufunsa funso.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:17

17-Yesu atawuyamba ulendo wache, munthu wina wache anamuthamangira, namugwadira Iye, namufunsa kuti, "Mphunzitsi wabwino," ndichite chiyani kuti ndilandire moyo osatha?"

-Kodi funso limene mnyamata wa chuma anamufunsa Yesu linali lotani?
-"Kodi ndiyenera kuchita chiyani kuti ndilandire moyo osatha?

-Kodi chenicheni chimene munthu ameneyu ankamufunsa Yesu chinali chiyani?
-Ankamufunsa Yesu za ntchito zabwino zimene iye ankayenera kuchita kuti akalandile moyo osatha.

-Kodi tingalandile moyo osatha chifukwa cha ntchito zathu zabwino?
-Ayi.

-Kodi nthito zathu zabwino zingalipilire moyo osatha?
-Ayi.

-Kodi Yesu anayankha chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:18

18-Yesu anayankha kuti, "Kodi chifukwa chiyani ukunditcha Ine wabwino? Palibe wabwino, koma m'modzi yekha – ndiye Mulungu.

-Yesu anamufunsa munthu uja kuti chifukwa chiyani ankamutcha Iye wabwino.
-Kenako Yesu anati kuti palibe wabwino koma Mulungu yekha.

-Kodi Yesu ankakana kuti Iye sanali wabwino?
-Ayi.

-Kodi Yesu ankakana kuti Iye sanali Mulungu?
-Ayi.

-Kodi nanga  chifukwa chiyani Yesu analankhula zimene analankhulazo?
-Yesu ankafuna kuti munthu uja amvetsetse kuti chifukwa chakuti anthu onse anabadwira mu tchimo, palibe munthu wabwino.
-Yesu ankafuna kuti munthu uja amvetsetse kuti chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene alibe tchimo, Iye ndiye wabwino.

-Mnyamata wa chuma uja ankaganiza kuti angapeze moyo osatha pachita ntchito zabwino.

-Kodi chimene sanamvetsetse munthu uja ndi chiyani?
-Munthu uja sanamvetsetse zakuti ntchito zathu zabwino sizingathe kusitha kuyipa kwathu kuti tikhale abwino.

-Munthu uja sanamvetsetse zakuti ntchito zathu zabwino zimene timachita panja, sizingathe kusintha mitima yathu yoyipa imene ili mkati.

-Apa pali chitsanzo:

-Kodi ngati chipatso chili chowola mkati, ife tingathe kuchisintha pochitsuka panja?



-Ayi.
-Chipatsocho chikhalabe chili chowola mkati mwache.

-Kodi ngati chipatso chili ndi mphutsi mkati mwake, ife tingathe kuchisintha pochipukuta panja pache?
-Ayi.
-Chipatsocho chikhalabe ndi mphutsi mkati mwache.

-Munthu uja sanamvetsetse zakuti iye anabadwa ndi mtima okhala ngati chipatso chowola ndipo chodzadza ndi mphutsi.

-Ngakhale kuti munthu uja ankayesa kuchita ntchito zabwino panja pache, zimenezi sizinathe kuwusintha mtima wache oyipa umene unali mkati mwache.

-Yesu ankamuphunzitsa munthu ameneyu kuti palibe munthu amene ali wabwino chifukwa chakuti anthu onse anabadwa ndi mitima yowola.

-Chifukwa chakuti mitima yathu inabadwira mu tchimo, palibe ntchito zabwino zimene zingathe kuyisintha mitima yathuyi.

-Sitingakhale anthu abwino pochita zinthu zabwino.
-Ntchito zathu zabwino sizingatipangitse ife kukhala abwino.

-Kodi kenako Yesu analankhula chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:19-20

19-[Yesu anati] “Ukuŵadziŵa malamulo: Usaphe, usachite chigololo, usabe, usapereke umboni onama, usanyenge, lemekeza atate ako ndi amako.”